# MAWU A MLEMBI

# WAMKULU MU UNDUNA WA MAGETSI

# PA MWAMBO OYATSA MAGETSI

# M'BOMA LA CHITIPA

# PA

# THAZIMA TDC

# PA $1^{ST}$ JUNE, 2020

- **Ulemu kwa anduna athu Olemekezeka Atupere Austin Muluzi;**
- **Ulemu kwa Mayi Chimwemwe Gloria Banda, Mkulu woona zogawa magetsi ku unduna wa magetsi**
- **Mkulu wa Kampani yogawa magetsi (ESCOM);**
- **Mkulu wa Kampani yopanga magetsi (EGENCO);**
- **Mkulu woona za mafuta m'dziko muno (NOCMA);**
- **Mkulu wa Kampani yogulisa magetsi (PML);**
- **Olemekeza phungu wadera lino komanso aphungu onse muli pano**
- **Bwana mkubwa wa boma lino Bambo a Fred Movete.**

- **A Paramount Chief Chikulamayembe ndi mafumu onse mwabwera pano;**
- **Akuluakulu a Boma;**
- **Mamembala a Nyumba zofalitsa mau;**
- **Amayi ndi Abambo.**

**MONI NONSE!!!**

Amayi ndi Abambo, lero tasonkhana pano pa Thazima Primary School ngati umboni wa ntchito yabwino yomwe Unduna wa za magetsi ukugwira motsogozedwa ndi mtsogoleri wadziko lino Professor Arthur Peter Mutharika. Kotero kuti malo ano ndi malo oyenera kukhala anthu achimwemwe kwambiri lero chifukwa tikuyatsa magetsi omwe anthu mwakhala mukuwayembekezera.

Ine ndili osangalala kwambiri pozindikira kufunikira kwa magetsi kwa ife anthu. Choncho ndiyamike boma chifukwa likukwanilitsa njira zothandizira kutukula dziko lino popereka magetsi kwa anthu m'madera onse kuphatikizapo madera akumudzi.

Wolemekezeka anduna, ndikuthokezeni mwapadera kamba ka chidwi chomwe muli nacho popeza nthawi kudzayatsa magetsi kuno chifukwa mwasiya ntchito zina zochuluka zomwe inu mumachita potumikira anthu mdziko muno. Koma mwapeza nthawi kubwera kuno lero zomwe zaonetseratu chidwi chomwe boma motsogozedwa ndi mtsogoleri wadziko lino Professor Arthur Peter Mutharika alinacho chofuna kutukula a Malawi okhala madera akumudzi.

Olemekezeka amayi ndi abambo, boma motsogozedwa ndi Mtsogoleri wadziko lino Professor Arthur Peter Mutharika likugwira ntchito yayikulu ndi yotamandika kuonetsetsa kuti magetsi afika m'madera akumidzi.

Amayi ndi Abambo, magetsi ndi awa afika koma tiyeni titsatire ndondomeko zoyenera kuti tifikitse magetsi mu nyumba zathu. Magetsi ndi abwino koma kupanda kusamala amapha komanso kuononga katundu. Tiyeni tiafunse a ESCOM kuti atithandize kulowetsa magetsiwa mwaukadaulo kuti tipewe ngozi zimenezi.

Pomaliza, amayi ndi abambo, ndipemphe atsogoleri, azipani, ogwira ntchito m'boma, mafumu komanso makolo kuti muwonetsetse

kuti tikusamala zipangizo zamagetsi. Tiyeni tikhale alonda a ife eni, ndipo omwe angapezeke akuba zipangizozi tiwagwire nkukawapereka ku polisi. Tikatero chitukuko chipita patsogolo mdera lathu lino. Tiyeni tisamale katunduyu ndi wandalama zambiri komanso opindulira ife tomwe kwathu kuno.

Amai ndi abambo, ndi mawu ochepa amenewa ndiloleni ndidzutse anduna athu kuti atiyankhule.

***Zikomo Kwambiri.***